

Uzimu Weniweni - Zolembedwa mu Chichewa

Gawo 4: Mmene Mungadzimvetsetsere Inu Eni

Zolembedwa ndi Chip Ingram

Pali zinthu zambii zimene akatswiri a za maganizo ndi a za uMulungu samagwirizana kwathunthu. Koma akatswiri a za maganizo ndi akatswiri a za uMulungu amagwirizana kuti kuchokera pa nthawi imene tinabadwa mpaka pa tsiku limene tidzafe, timayamba kuyesa mozindikira kapena mosazindikira kuyamba kufunsa ndi kuyankha mafunso atatu. Funso loyamba: Kodi ndine ndani? Funso lachiwiri: Kodi ndili mbali iti? Ndipo funso lachitatu: Kodi ndikuyenera kuchita chiyani? Izi ndi zinthu zimene zimakhudza kudziwika kwathu, chitetezo chathu ndi kufunikira kwathu.

Tingathe kuyitchula mitundu yonse ya zinthu zosiyanasiyana, Koma Yesu anachipanga chomveka bwino, “Konda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse ndi maganizo ako onse, ndi mphamvu zako zonse ndi kukonda mnzako monga udzikondera iwe mwini.” Ndipo mu Aroma mutu 12 akupereka chithunzithunzi cha mmene atsatira Khristu weniweni amaonekera mmoyo wake wat siku lirilonse.

Mwa mawu oti Mulungu okonda, Paulo akuti; Kodi mumakonda bwanji? Kodi chimene Mulungu amafuna kwambiri kuchokera kwai unu ndi chiyani? Amafuna inu ndi ine, zonse zimene tili nazo. ziperekedwe kwa Iye. Ndiye kenako pozindikira kuti ndi nkondo ndipo mayendetsedwe a dzikoli amafuna kukopa mtima wathu kuchokera kwa Mpulumutsi wathu, Amafuna ife kukhala olekana kuchoka ku machitidwe a dziko.

Tsopano tisuntha kuchoka pa ndime 1 ndi 2 kupita pa ndime 3 mpaka 8. Pano pali chinthu chimene tiphunzire. Kodi mumagwira bwanji chenicheni chimene inuyo muli? Simungakonde ndipo sindingakonde anthu ena ngati simudzikonda inu eni ake. Sindikutanthauza kuti ndi zachabechabe. Ndikutanthauza mu njira ya thanzi. Kodi mmayang’ana bwanji pa kalilore, osati thupi lathu, koma pa kalilore wa moyo wanu, mmakumana ndi amene inu muli weniweni, ndi kunena kuti, “chipangidwe changa ndi choopsa ndi chodabwitsa. Ndine wofunika. Mulungu ali ndi dongosolo la moyo wanga. Sindine wamfupi kwambiri, sindine wamtali kwambiri. Ndili ndi umunthu woyenera. Ndili ndi mphatso zoyenera. Sindisowekera kukhala ngati wina aliyense.

Pano pali choonadi cha nkhani: ambiri a ife, anthu ambiri mdziko lonse lapansi, amaononga nthawi yambiri ndi mphamvu zawo kuyesera kukhala winawake kapena kulakalaka kuti akadakhala winawake. Ndiye koteri timavala monga ngati winawake, timachita ngati winawake, tili ndi anthu osiyanasiyana amene timawasilira. Ndiye timaononga mphamvu zathu zonse ndi nthawi yathu kuyesera kukhala wowoneka ngati iwowo kapena chinthu china chake chimene chili pafupi kwambiri mooneka bwino ngati

munthu yekhayo wapaderadera munatindi wa anthu mabilyoni asanu ndi awiri a anthu a pa dziko lapansi amene ali ndi DNA yapaderadera ya inu. Ndipo munapangidwa ndendende mmene inuyo mulili ndi Mlengi wa zonse za moyo, chifukwa ali ndi dongosolo la inu, ndipo Anakudalitsani ndi mphatso, ndipo Akufuna kuchita chinachake chachikulu mwa inu, kenako chinachake chofunikira kwambiri kudzera mwa inu.

Lero tifunsa ndi kuyankhka funso. **Kodi mmagwira bwanji chenicheni chimene inuyo muli?** Tsegulani notsi zanu zophunzitsira, ngati mungathe.

Funso loyamba. Kodi ndine ndani? Pomwe munali ang'ono munaphunzira msanga mmakhala mubanja. Ndine ndani? Ndine Ingram! Abambo anga anaonetsetsa kuti ndimvetse kuti dzinali ndi lofunikira kwambiri. Kotero kuti sinayanere kutulua kunja ndi kukapanga chinthu cinachake chimene chikadachititsa manyazi zina la Ingram. Mumayamba kukula pang'ono ndipo amati, “Ndinu ndani?” Ndipo kawirikawiri timapereka ntchito yanu kapena zimene timachita. Chabwino ine ndi wa sayansi ndine injiniya wa komputa, ndine mayi wapakhomo, ndine mmisili wa zomangamanga, ndine wa za magetsi. Ndipo kutero, ndine ndani. Kudziwika kwanga kumatengera zimene ndimachita.

Monga mmene tikukulirabe kapena monga moyo umasinthira kawirikawiri, kenako zimakhala zokhudza zimene timakonda; “Ndine mayi, Ndine wosambira, ndine wojambula.” Koma zonsezi zimabwerera kufungo limenelo – kuchokera muli mwana kufikira kumapeto a zaka zanu za chisodzera kuifika kuyamba ukulu wanu. Kenaka makamaka kusintha kochepe kwa moyo wapakati, ndine ndani? Kodi kudziwika kwanga ndi kuti? Nthawi zonse mmafunsa funso limeneli. Momwenso, iwo amene ali makolo, chomwechonso ana anu.

Funso lachiwiri lalikulu limene nthawi zonse timafunsa: Kodi ndi mbali iti? Ili ndi lokhudza chitetezo. Mukukumbukira muli ku sukulu mukukhala mmagulu, sizachilendo, pa sukulu iliyonse muli ndi othamanga, a misala, gulu la anthu ofatsa, gulu ala anthu a “mkati” ndi gulu lenileni la anthu a “kunja”. Ndiye kenako kunali makalabu, choncho mumalowa makalabu osiyanasiyana. Kenako nthawi zina kumbali kumene ndili ndi zokhudza mtundu wanga, anthu amene amawoneka ngati ine.

Kapena nthawi zina zimakhala zokhudza kumene tapezeka, ndine mbusa, ndine wogwira ntchito mongodzipereka, ndine waphunzitsa masewero, ndine mphunzisti, si choncho? Nthawi zina kumene ndimapezeka ndi kwabwino. “Ndili mukalabu ya kumudzi ndipo anthu ngati ine amakonda kupita kumeneko.” Kapena ndine wa gulu ili chfiukwa ndimavala zovala zanga ndi zokongol mnjira iyi.

Muyenera kumvetsetsa kuti mphamvu zomwezo munagwiritsa ntchito muli wachichepele kapena mmbuyo mwa moyo, mu chimodzi cha zimenezo, ndi choonadi chimene munthu wina aliyense anapangidwa ndi Mulungu wolenga zonse ndi chosowa chofuna kukhala ndi mbali, choswekera kumvetsetsa chimene inu muli enieni. Ndipo timadutsa mwa njira zina, nthawi zina zimene ndi zosagwira ntchito. Moonadi - nthawi zina ndi zoopsa kwambiri.

Funso lachitatu tikufunsa ndi ili: **Kodi chifukwa chiyani ndili pano? Kodi ndikufunika ndichite chiyani?** Ndi chofunikira. Kotero ndi chofunikira kwambiri ndi chothetsa nzeru kotero, nthawi zina timawomba kudutsa apa. Kodi ndi liti lomaliza limene munayima ndi kunena kuti, “Chifukwa chiyani ndili pano pa dziko lapansi? Kodi tanthauzo la moyo ndi chiyani kwa ine?

Onani, ine kumanzere kwai ne, ndi inu kumanzere kwa inu. “Chabwino, inde, ndikutsimikiza kuti ndi funso lofunikira kwambiri mmoyo, kotero ndizungulira pamenepo, koma ndimalandira ma voicemails ambiri, mukudziwa, ndimalandiranso ma e-mail ambiri, ndipo mukudziwa, pali ntchito, komanso pali ana amene ayenera kusamalidwa ...”

Ndipo ndizodabwitsa mmene anthu ambiri amawombola kudzera mmoyo kukwaniritsa ntchito za mitundu yonse, kuyankha mitundu yonse yazokhumba zimene kwenikweni ndi zakhudza kudziwika ndi chitetezo, ndipo mmumadzadzuka patatha zaka 30, 40, 50 ndipo mmadzazindikira kuti moyo wanu wonse mwakhala wogayika. Moyo wanu wonse wakhala chinthu china chake chimene chizachtike tsiku lina mnjira ina yake kunjako. Ndipo simunasiye kufunsa. Kodi ndikofunika kuchita chiyani ndi moyo wanga?

Gawo lalikulu la pakati pa zaka za moyo ndi choskonezo ndi anthu kuyang’ana pa kalilole wa mbuyo ndi kunena, “Sindinagofuna funso limenelo, pomwe ndyamba kuganiza za ichio mozama, sindikonda yankho lake chifukwa sikuti sindikungosandizwa kokha, koma sindinapereka mphamvu kapena nthawi kapena mbiri yakale ya chimene ndikuganiza kuti mwina mwake ndi chofunikira kwambiri.

Tsopano, musanazame pansi pa inu eni nokha, chifukwa kunenetsa, awo ndi akulu sichoncho kodi? Ndipo sizokondweretsa kuti nkhani zazikulu kwambiri mmoyo mwanu mungathe kuzipondereza pansi chifukwa ndi zovuta kwambiri kuyankha kwake. Kodi ndi ndani pano anganene, “Kodi ndine ndani weniweni ndipo ndili mbali iti ndipo kodi ndiyenera kuchita chiyani? Onani, mungathe kupeza china chake mwamphamvu? Chabwino? Palibe mafunso akulu kuposera ili, ndipo pa namtindi wa anthu sanaganizrepo mozama kapena kukupatsani mayankho omveka bwino a zimenezi.

Koma ndiloleni ndikuuzeni chifukwa chiyani, Ndiloleni ndifotokoze chifukwa chimene iwo ali ovuta kuyankha. Chinachake chinachitika kwa makolo athu oyamba chimene ife tinatengera kuchokera kwa iwo chimene chimapangitsa kuti mafunso awa akhale ovuta kuyankha. Icho ndi chifukwa chimene dziko lapansi limakhala ndi chikoka chotero kwa ife. Ndi chifukwa chake timakhazikika pa yankho lachiphamaso ku zinthu zimenezo, kudziwa pansi pa mtima kuti sakwaniritsa kwenikweni.

Ndime ya Genesis 3 mutu wa 3, munthu okonda kwambiri, munthu wopereka kwambiri, munthu wopatsa zonse za moyo. Mlengi wa dziko lonse, Yawe Mulungu, analenga mtundu wa anthu ndi kuwawuza kuti zonse zimene lye ali nazo ndi chilichonse chilipo kwa iwo. Pali chimodzi chokha choletsa, musadye kuchokera ku mtengo. Ndipo makolo athu, poyamba ponamizidwa, ndiye kenako pochita mwa chifuniro anawukira, ndipo tchimo linalowa mu dziko lapansi. A za uMulungu amachitcha, “Kugwa kwa munthu.” Ndipo tinatenga nkhaniyo ndipo tinapeza chimene chinachitika. Ndipo pamene tikutenga nkhaniyo mudzazikirira chifukwa chake inu ndi ine, ndi chovuta kwenikweni kuyankha bwino mafunso amenewo.

“Anamva kuyenda kwa Ambuye Mulungu mmundamo mkati mwa tsiku lokongola, mwamuna ndi mkazi wake anadzibisa okha kuzemba pamaso pa Ambuye Mulungu mkati mwa mitengo ya mmunda.” Kunali kwa nthawi yoyamba izi kuchitika. Amathamanga kukakumana Naye. Amakhala pa malo angwiro. Mmaganizo mwao anali a maliseche, mu uzimu anali a maliseche, kuthupi anali a maliseche. Ena a za uMulungu amaganiza kuti panali mphamvu ya kuwala imene inawachokera asanagwe mu uchimo. Panali ubwenzi wathunthu ndi Mulungu. Ubwenzi ndi kusatetezeka ndi wina ndi mnzake, kuvomerezana kopanda malire. Moyo unali wangwiro.

Ndipo tsopano akumva Mulungu akubwera ndipo kwa nthawi yoyamba, anabisala. “Kenako Mulungu anayitana mwamuna ndi kunena kwa lye, “Uli kuti?” M ongdziwa, ili silinali funso longofuna kudziwa. Ili linali lofufuza. Mulungu anadziwa kumene anali. lye amadzafunsa ndandanda wa funso kuthandiza Adam kuzindikira penipeni pamene iye ali. Adamu anati, “Ndinamva mawu anu mmundamu, ndipo ndimaopa chifukwa ndinali wamaliseche, ndipo ndinabisala.”

Ngati muli ndi cholemba, mungathe kuchitenga, ndipo muzolemba zanu, muzungulize mawu akuti “Ndimaopa”, “Maliseche”, ndi “Kubisala”. Izi zidzabweranso. Mudzazipeza mu dongosolo logwirizana limene muli nalo ndipo ine ndili nalo ndi munthu wina aliyense ali nalo.

Ndipo Mulungu anati, “Ndani anakuuza iwe kuti uli wamaliseche? Kodi wadya za mtengo uja umene ndinakuuza iwe kuti usadye? Ndipo kotero anayankha Mulungu,

ndipo ndi zodabwitsa ngati inuyo mukanakhala imkazi wake, iyi sinthawi yabwino. Chimene inu mudzaphunzire inu ndi chakuti simangamukhulupirire munthu uyu. Kwa nthawi yoyamba, kodi chimene inu mudzaphunzira chiyani, pamene mwapanikizdwa, chimene iye achite, mmalo movomereza kulakwa kwake, akukhala wolandira ndipo akukukankhira mlandu kwa inu.

Ndipo mwina mwake Hava wayima pamenepo, kudziwa nkhani yonse, ndipo iye adzamva mwamuna wake akunena kwa Mulungu, “Mkazi amene munandipatsa ine kuti akhale ndi ine, ameneyo anandipatsa ine za mtengo, ndipo ndinadya.” Kumasulira; Sikulakwa kwanga, Inu ndinu amene munandipatsa iye kwa ine.

Ndipo Mulungu akupitiliza ndi kulondoloza mafunso a kufufuza, “Ndipo Yehova anati kwa Mkazi, ‘Chiyani chimene wachita? Ndipo anati mkaziyo,’ kuwerenga mwa changu, “Njoka inandinyenga ine ndipo ndinadya.” Mmau ena, sikulakwa kwanga. Ndi kulakwa kwa njoka, ndi iye amene anapanga munda uwu ndi amene anapanga njoka?

Ndipo mukudziwa chiyani, mavuto onse a mmoyo uno ndi a Mulungu. Ndi zodabwitsa kuti zambiri sizinasinthe. Pomwe pachitika ngozi, pomwe pali zovuta, pomwe china chake chachitika mu dziko lapansi, chimene ndimamva nthawi zonse ndi: Kodi Mulungu walola bwanji kuti izi zichitike? Kodi Mulungu wandipatsa bwanji ichi? Sitilemba chabwino chili chonse chimene lye watichitira, koma ngati chinachake chalakwika, timamuyimba lye mlandu.

Pali zotchinga zitatu zimene mudzaone mundime imeneyi zokhudza chifukwa chimene ndi kovuta kwambiri kugwirizana ndi iwe weniweni. Choyamba, ndi mantha okhazikika mizu yake mu manyazi. Onani iye akuti “Ndimawopa.” Chabwino. Chifukwa? “Ndimawopa,” chifukwa tsopano kwa nthawi yoyamba Adam anazindikira kuti anali wa maliseche. Komabe, linali thupi, koma chabwino kudutsa pamenepo ... anazindikira kuti wayikidwa poyera. Chimene anazindikira, pomwe anakumana ndi maso a winawake amene amaona mwamtheradi mwagwirowo chilichonse chimene sangathe kuyesa kwake.

Pali kudzimvera chisoni kumene kunachitika. Ndipo ndingahte kukuwuzani kuti umu ndi mmene timachitira kawirikawiri ndi Mulungu ndipo umu ndi mmene timachitira ndi wina ndi mnzake? Tanthauzo loyamba la kulumikizana ndi anthu ena ndi Mulungu ndi mantha, ndipo mizu yake ndi manyazi.

Onani, ngati tingapeze ukadaulo wachipha maso ndi zonse za mmaganizidwe mu njira yathu, ngati tingachotse onse za maonekedwe mmoyo mwanu ndi mwanga, ndi zonse zakasamalidwe za mafano, ndi zonse zachimango cha zinthu, ndi miyeso yonse

yodzikanana imene muli nayo. Pansi pa mtima wanu ndi moyo wanu, ngati wina wake akudziwa zonse za inu, ndikutanthauza, inu nonse, maganizo, nsanje, zolinga, zinthu imene munaganiza osayiwala zinthu zimene mwachitapo, pansi pa mtima mwanu, mwatsimikizidwa bwino kuti mungakanidwe.

Ndipo kotero timalumikizana wina ndi mnzake mwa mantha ndi kutenga mphamvu mopitilira malire kuyima ndi kukonza maonekedwe athu. Ndipo pakuti tilibe kutsimikizidwa kwakuti ndife ndani kwenikweni, timafuna kukondedwa ndi anthu ena. Ndimazitcha mtundu wa umunthu. Chifukwa cha maziko anu, ndi mphatso zanu, ndi dera la dziko limene inu mwakulira, ndi anthu mmagulu ena apadera, ndipo kotero mumaphunzra mmene mungachitire motero, ndi kuvala monga iwo, ndi kusowekera kuyendetsa icho, ndi ana anu ayenera kuphunzira sukuli monga yomweyi. Ndi kukhala ndi zinthu izi zonse zimene mwina mwake, mnjira ina yake, ngati zonse zayikidwa pa mnzere, chifukwa chitsimikizo chanu chimachokera mmenemo. Mumapeza kuvomerezeka kuchokera mmenemo. Mumasiliridwa ndi anthu.

Pano pali vuto: Chimene mukudziwa inu mu mtundu uwu ndi chakuti mukuzijudula mwa munthu uyu amene ali ndi zonse pamodzi ndipo ndi wokonda ndi wokoma mtima ndi wabwino mu china chili chonse. Mukudziwa pansi pa mtima wanu kuti kwanikweni sizikuyimira zonse zimene inu muli weniweni.

Ngakhale pomwe anthu angakonde mtundu, simupeza chikondi chifukwa mumadziwa kuti sindinu. Ndipo icho ndi chifukwa tapeza ena a anthu amene ali okongola kwambiri ndi opambana kwambiri, timapeza achita zinthu zodzetsa tsembwe ndi kunena kuti, “Kodi zikutheka bwanji kuti munthu amene ali ndi zinthu zonse amazilakalaka amadzipha kapena kuwononga moyo wawo ndi chizolowezi choipa chokanika kuchisiya. Ndi zonse izi zotsutsana mu mtima mwawo, ndi mantha okhala ndi mizu mmanyazi.

Onani chinthu chachiwiri chimene chimachitika. Sanangonena kokha kuti, “Ndimaopa,” akuti “kubisala” – kuzikika mu kusowa chitetezo. Onani, pomwe muli a maliseche, mumamva kusatetezedwa. Mumamva kusakwaniritsidwa ndipo mumabisala. Sitimangokhala a mantha okha, koma ndimadzibisa ine weniweni kwai nu, ndipo inu mumabisa inu weniweni kwa ena ndi kwa Mulungu.

Sizikondweretsa pomwe simumva mkati mwanu kuti mupemphere, makamaka pamene pansipansi mukumva kuti motero, mukudziwa kudzitsutsa kwa mulingo wotsika mkati mwa mtima wanu? Mwina mwake simachimo akuluakulu, koma a mtundu wochepawa amayamba kuwunjikana ndipo kenako simulimbikitsidwa kuti mupemphere. Sindikudziwa za inu, koma chimene ndazindikira ndi chakuti sindikufuna kupita

koyankhulana ndi Mulungu tsopano lino chifukwa ndikudziwa mmene zikathere. Zoonza? Akundipangitsa kukhala wowonadi, kuyika poyera chenicheni chimene ine ndili, ndipo sindikonda zimenezo. Ndiye koteri ndimasewera sewero ili. ‘Chabwino ngati sindingayankhuledi ndi lye mozama tsopano, lye sakudziwadi’

Koma kodi mumachita izi ndi anzanu, kwa inu amene ndinu wokwatira? Kodi mmachita izi ndi amene mmagona nawo chipinda chimodzi? Kodi mmachita izi ndi anzanu zedi? Kodi mmasewera masewero amenewa? Tili ndi mantha amene anazikika manyazi, ndiye kenako timabisala mukusowa chitetezo chathu.

Ndipo ndingakuwuzeni inu china chake? Pano pali uthenga wabwino oti muphunzire. Uwu ndi uthenga wakumasulidwa kwa ine. Aliyense pa dziko pano ndi wosowa chitetezo mwakakasi. Ndipo ngati mukunena kuti “Oho ayi, sindikudziwa ngati ndingagule icho,” chabwino, ndiloleni ndikuwuzeni ka nkhanu kakang’ono kamene kanali kondimasula ine.

Malo oyambirira amene ndinali ndi mwayi wotumikira ngati mbusa. Ndinali ndi zaka 28, ndipo unali mpingo waung’ono mmalo mwa chimpingo chachikulu, unali kumudzi pamunda wa pafupifupi mailosi 30 kunja kwa Dallas, Texas. Tawuni yonse inali ya anthu pafupifupi 3000, ndiye kenako panja pa tawuniyo panali nyumba yaying’ono yomangidwa yoyera imene inali tchalitchi chathu ndipo tinali anthu 35. Unali ubusa wanga woyamba ndipo sindinadziwe chimene ndimachita, koma awa anali malo amene Mulungu anandiyitanira. Ndipo ndinaganiza kuti ndi tchalitchi cha kumudzi chifukwa chakuti anthu anali ndi magalimoto ndi mfuti kumbuyo kwa magalimoto awo, ndipo onse anali ndi munda ikuluikulu ya ziweto ndi akavalo.

Koma patatha pafupifupi miyezi iwiri ndili kumeneko, pomwe ndinayamba kuyendera anthu mmakomo mwawo, si makomo okhawo amene anali ndi nyuzipepala ya Southern Living pa tebulo lawo la khofi, makomo awo anali a nyuzipepela ya Southern Living. Ndipo mukudziwa, kunali anthu 35 okha, koma munthu uyu anali mwini wogulitsa Honda, wogulitsa Yamaha, anali ndi nyumba zambiri mtawuni ya Austin ndi mafuta a galimoto.. Ndipo munthu uyu anali mwini wa kampani ya “insurance” Sindikudziwa mmene mmachitira zimenezo koma wina wake anayenera kukhala mwini wakem wa zinthuzo, ndikuganiza choncho. Ndipo munthu winayo cha apo anali ndi makampani akulu kwambiri a zowerengetsera ndalama mtawuni momwemo.

Ndipo mwadzidzidzi ndinazindikira kuti ine wochokera ku banja la pakatikati, makolo onse anali aphunzitsi a ku sukulu, ndipanga ubusa kwa anthu 35, koma olemera kwambiri zedi, anali olemera kwambiri kuyerekeza ndi kumene ine ndimachokera.

Ndipo ndinali wochititsidwa mantha. Kodi munayamba mwakhalapo ndi winawake amene amakupangitsani inu kukhala operewera?

Ndimamva kuchepa, ndipo ndimayamba kuganiza ndine wopanda nzeru, ndi kudziwa kuti anali anzeru kuposa ine, ndipo ali ndi katundu yenseyu. Kwa chaka ndi theka choyamba, ndikukumbukira ndinali mmaso, ndikutanthauza kuti sindinagone mkomwe mausiku onse oyamba asanu ndi limodzi kapena asanu ndi awiri. Ndisanapereke uthenga wanga woyamba nditangodziwa kuti anthuwa ndi ndani chifukwa ndimamangika kwambiri za zimene anaganizira za ine.

Ndipo kenako Miulungu andipatsa Bukhu lolembedwa ndi katswiri wa zamaganizidwe wa ku Switland, wa za maganizidwe wa Chikhristu wotchedwa Paul Toumier. Simukuyenera kuwerenga bukhulo. Mwina mwake silitsindikizidwanso. Linamasulidwa kuchokera ku chilankhulo cha French kupita ku chingerezi. Mutu wa bukhulo ndi *The Strong and the Weak*. Ndipo anali atalangiza anthu kwa zaka 30 kapena 40, ndipo ndemanga yake inali yosavuta. Aliyense pamaso pa dziko anali wakakasi ndi kudzimva kuperewera. Anthu ena amasonyeza kudzimva kuperewera kwawo mwa kuchita kwamphamvu kwa zinthu. Amadzilimbitsa. Amakuwuzani kuti iwowo ndi ndani, kumene akhala. Amavala zodula. Amakuwuzana anthu amene amawagwirira ntchito, ndi makalata angati olembedwa mdzina lawo. Makhozedwe a mayeso a ana awo. Mukayamba kuwadutsa amakwiya ndipo amawonjezera mphamvu, ndipo mwadzidzidzi mumamva kuchepetsedwa ndi kubwerera.

Ndipo anthu amene amamva kuperewera mwakakasi amene amadzipatsa mphamvu, talotani chimene amachita? Amadzipatsa mphamvu pochita molimba kuti apereke danga loti musayandikane chifukwa pansi pa mtima wawo ndi anyamata kapena atsikana ang'ono a mantha, monga ngati mmene wina aliyense alili. Amabisalira. Amakhala kuti ali ndi masamba a mkuyu wosiyana ndi anthu ena.

Ndipo apa, muli ndi anthu ena amene ali ndi kuchita modzichepetsa. Ndipo amayang'ana kwambiri pansi pa phazi lawo ndi kunena kuti, "Palibe chilichonse chimene ndingachite ndipo sindine woyenera. Ndinakumana ndi zinthu zoopsa kwambiri. Ndadutsa mu zinthu zambiri ndipo inu mwina mwake simungathe kuzimvetsetsa." Ndipo pomwe mukuyamba kukumana nawo mumayesetsa kuwathandiza iwo.

Kenako mmayesetsa kuwathandiza iwo. Ndipo kenako amakhala ndi chojambulira mmutu mwawo: Ndine wozunzidwa, moyo ndi wowawa, ndine wosayenera, ndine munthu woyipa kwambiri, palibe amene angandikonde ine. Ndipo patatha mkumano

isanu mumati, “Kodi mukudzwa chiyani, mwina mukhoza kukhala olondola.” Zoona? Mukudziwa chimene ndikutanthauza?

Ndipo ndiye safuna chithandizo. Amafuna kumveredwa chisoni ndi kuwonedwa, koma akachita choncho, zimabweretsa kutalikirana. Umakhala uneneri wodzikwaniritsa okha. Amapeza njira yakuti anthu anene, “Sindiyandikana ndi inu.” Zimagwira ntchito. Koma pali kusiyana pakati pa ziwirizi, ndi kuchita mwamphamvu ndi kuchita modzichepetsa.

Nthawi zambiri ndinali pakati pa anthu amene amadzikweza ndipo ine ndinali ndi mantha owopsa, ndipo ndinawerenga bukhulo ndipo getsi lowala linathima. Ndikukumbukirabe kwa nthawi yoyamba yokumana ndi munthu uyu pa mfwitsulo, ndipo anayamba kundiuza izi ndipo ine ndinali kufufuza za ichi ndipo ndidzachita zimenezi.

Ndipo ndinatsamira mmbuyo ndikuganiza kuti munthu uyu akumva kuperewera kwambiri. Ndipo kenako ndinadziwa za baja lake ndi mavuto ake ndi kuyamba kulangiza ena a ana ake. Ndipo ndikukumbukirabe kuganizira anthu awa ndi wosokonokera monga ngati ine. Moonadi, ndikuganiza kuti ndalama zingakupangitseni inu kukhala osokonekera kwambiri.

Ndipo ndinaganiza zakuti ndisiye kungoganizira. Ndinavula chigoba changa pa mulingo watsopano ndi kuwapanga kukhala anzanga. Ndipo ndinawona Mulungu akuchita chozizwa. Anapanga chozizwa mwa iwo, ndipo lye anapanga chozizwa chachikulu mwa ine. Ndipo ulendo umenewo woyambirira unandiphunzitsa kuti aliyense amamva kuperewera kwambiri.

Ndipo mumaphimba mu njira ina yake. Mdimaphimba mu njira ina, ena amaphimba ndi zimene achita ndi mmene amachitira ndi chipambano chawo, ndipo anthu ena ndi nkhani zawo zimene amanena. Koma mukudziwa inu; chimatchedwa “kugwia.” Mumalumikizana mu magawomagawo, mu njira zazing’ono kapena zazikulu chifukwa cha mantha, ndipo mmalumikiza ndipo ndimalumikiza pobisala. Ndipo timabisala chifukwa ndife operewera.

Chotsatira chachitatu kuchichita ndipo chifukwa ndi kovuta kuyankha mafunso awa ndi **kukanirana kozikika mukukana**. Mwamuna akuti, “ndi mkazi” Mkazi akuti, “ndi njoka”. Koma mapeto ake, onse akukanira Mulungu. Pamene tikukamba za Aroma 12:3-8 kwenikweni akuthandizani kuzindikira amene muli, mbali imene muli, ndi chimene mukuyenera kuchita.

Ndime 3 idzatiuza mukamphindi kuti inu ndi ndani, ndime 4 ndi 5 idzakuuzani kumene muli, ndi ndime 6 mpaka 8 idzakhala kuyamba kwa kumvetsetsa kwenikweni kwa udindo wanu ndi chimene inu muyenera kuchita.

Koma ndikufuna kukuwuzani nkhani yotsatira inayo, chifukwa ndi chinthu china kunena kuti, chabwino, aliyense ali operewera mwakakasi. Kodi mmachita chiyani ndi zoterozo? Ndikutanthauza, ndipatseni china chake chindithandizire ine chifukwa chilankhulo cha thup lanu muchipinda chino panopo, simukunena, “Oho, eya, zimenezo ndi zoonadi,” koma mwatsala pang’ono kupatula gawo laling’ono la inu ndi kunena kuti, “Hii, sindikuganiza kuti akuyankhula ndi ine. Zoonadi?”

Zayenera kukhala zaka 10 mpaka 15 zinapita ndipo ndikupitilizabe ulendowu. Mooanadi, pa kadi lachitatu pa makadi asanu amene anali makadi anga amene ndimakhumba kukonzanso mtima wanga, ndinalamba zitatha zimenezo. Ambuye, ndikulakalaka kukhala weniweni kwambiri mu maubale alionse mwa mphamvu zanu ndi mwa chisomo chanu. Patatha zaka 15, kumene ndimatumikira ngati mbusa malo anachepa, ndipo mmodzi mwa anthu opanga malonda anayamba kuyika maulaliki anga pa wailesi ndipo sipanapite nthawi anali mnyumba zowulitsira mau zosiyanasiyana.

Ndipo ndiyitanidwa, kumene mapeto ake ndinazindikira kuti chinali chakudya cha madzulo chapamwamba kwambiri. Chinatchedwa National Religious Broadcasters, ndipo kunali mwina mwake anthu 20 kapena 30 oyambirira amene ndi olankhula otchuka mu America ndi akazi awo ku chakudya cha madzulo chimenechi. Sindinadziwe amene ndinali nawo pa chakudya chimenechi. Pa nthawi imeneyo timaulutsidwa mnyumba zowulitsira mawu 10 zokha. Kunali anthu ngati Chuck Swindoll, amene amapezeka mu nyumba iliyonse yowulitsira mawu, ndipo walemba mabuku 25 kapena 30, ndipo amafunidwa ndi nyumba yowulitsira mau ya Voice Of America.

Ndipo kotero ndinabwera ku chakudya cha madzulo ichi ndi mkazi wanga. Kupezeka kumeneko kunapangitsa mantha anga oyamba kuwoneka ngati, mukudziwa, masitepe a khanda. Ndiye kotero pa zinthu zonse, ndinakhala pansi, ndipo dzina limene linalembedwa pafupi ndi ine linali la Chuck Swindoll. Ndipo ndikuganiza, “Ooo, ayi.” Ndipo kotero mukudziwa, ndili ndi nthawi ndipo ndakhala pamenepo. Kwathu ndi ku California, ndipo mukudziwa, ndili mu tayi yanga ndi jekete, ndiye sindikukondwa ndi mmene ndavalira. Ndipo ndi zapamwamba ndipo ndi malodi a pamwamba. Ndipo Chuck Swindoll wakhala pansi, ndi ine ndakhala pansi. Ndakhala pamenepo kuganiza, “Kodi ndichite chiyani?” Chifukwa sindikuganiza kuti ndine woperewera koma kudziwa mmene panopa ndikumvera kuperewera.

Ndikulingalira- mu mtima mwanga mmene ndingachitire. Mwina mwake nditenga njira ya, “Heyi, Chuck, zikuyenda bwanji, Amuna inu?” Ayi, sindikuganiza kuti zimenezo zigwira. Bwanji zenizenizo, “Aaaah, Dr. Swindoll kodi utumiki ukuyenda bwanji?” Ayi,

sindikuganiza kuti izi zigwira. Ndikutanthauza, ndinali wamantha enieni. Sindinadziwe kuti ndichita bwanji pa malo pamenepo.

Ndinakumbukira ichi: Aliyense amamva kuperewera. Sindinathe kukhulupirira kuti iyenso angamve, koma ndikuganiza kuti Baibulo ndi loona. Kotero ndinangoganiza, ndigwiritsa ntchito zimene ndakhala ndikuphunzira. Ndiye ndinamugwira pa phewa anatembenuka, ndipo ndinati, “Aaaa, Bambo Swindoll, iyi ndi nthawi yanga yoyamba pamalo pano, ndipo ndikufuna kukuwuzeni, izitu zikundipinda mutu. Zikundipangitsa mantha. Sitili pa nyumba zambiri zowulitsira mau. Sindikudziwa mmene ndingachitire; sindikudziwa mmene ndingachitire pa za zowulitsira mawu. Mungandipatseko nzeru zina?

Ndipo sindidzaiwala, anakoka mpando wake kuyika mkono wake pa ine, ndi kuti, “Chip uzingoti Chuck.” Ndipo anayamba kofotokoza za ulendo wake kwa mphindi makumi atatu.

Ndipo kenako kwa zaka 6 kapena 7 ndinakhala ndikupita ku chakudya cha madzulo chimenechi – “Chip bwera kuno.” Ndipo amanena kuti, “Chabwino, ndiwuzeni chimene chikuchitika.” Ndiye kenako ndi kundiphunzitsa. Chifukwa chiyani? Ndikanatha kuyima. Ndikunena kuti, “Mukumvetsa kodi – tinali ndi nyumba yowulutsira mawu imodzi yokha basi. Pano tili pa nyumba zowulutsira mawu zisanu ndi ziwiri. Mukuganiza chiyani?” Ohoo, eya, dziko lonse lapansi, chabwino, izi zili bwino. Koma kodi mwamvetsetsa chimene chimachitika mukavula chigoba chanu ndipo ndinu weniweni basi ndipo ndinu woona ndi penipeni pamene inu muli? Kodi mukudziwa kuti ndi chiyani? Kodi mukudziwa amene akutuluka? Munthu wowoneka bwino kwambiri pa dziko lonse lapansi amene Mulungu anapanga ndi inuyo, **inu weniweni**.

Yang’anani zolembe zanu chifukwa ndikufuna kukutengerani pa ulendo wa ku mfundo zoyambirira za kudzizindikira kuti weniweni ndinu ndani, ndi malo amene inu muli, ndiye kenako chimene mukuyenera kuchita. Yankho la Mulungu ku dongosolo losagwira ntchito la kubisala, ndi manyazi, ndi mantha, ndi kukana ndi ili: “Kodi inu ndi ndani,” ndime 3, “Pakuti ndi chisomo chapatsidwa kwa ine, ndiwuza munthu aliyense wa inu, kuti asadziyese koposa kumene ayenera kudziyesa; koma aganize modziletsa yekha, monga, Mulungu anagawira kwa munthu aliyense muyeso wa chikhulupiriro.” Ngati muli ndi cholemba chija, chitengeni, lembani mnzere kungsi kwa mau akuti “ganizani” ndiye mukafika pa “ndiye muyenera” lembani mzere pansi pa awu akuti, ‘muyenera.” “Koma mmalo mwake ganizirani” lembani mnzere kungsi kwa “ganizirani” Kenako lembani mnzere pansi pa mawu akuti “chiweruzo chodekha”

Kotero muli ndi “ganiza, yenera, ganiza, ndi chiweruzo chodekha.” Mwalemba mnzere kungsi kwa “yenera’, chifukwa ndi mau enieni a chilankhulo, ndi mmene muyenera kuganiza, koma ngati mmene anamasulira ndi chongowerengera chosavuta, anadumpha mawu. Muzu wa mawu omwewo, “ganiza, ganiza, ganiza ndi chiweruzo chodekha,” onse ndi a muzu umodzi. Mawu akuti, “chiweruzao chodekha” akutipatsa ife nzeru yabwino kwambiri. Ndipo ‘musaganize za inu nokha monga wina amene ndi woledzera’. Pomwe munthu ndi oledzera, kodi amachita chiyani? Pamakhala mphamvu inayake yochokera kunja imene imalowa mkati mwawo imene imapangitsa iwo kuyang’ana moyo mnjira yakuti siyolondola.

Kotero amati, “Musaledzere ndi mayendedwe a dziko lapansi, musaledzere ndi chili chonse chimene banja lanu lakuwuzani.” Mukuyenera kukhala ndi kudzisanthula kwa inu eni kodekha. Mukuyenera kuganiza molondola kokhudza inu eni ake. Ili ndi lamulo loyamba. Mukufunika kufika pa mulingo wakuti muthupi, muubale, muuzimu, mmaganizidwe, mtima wanu ungayang’ane pa kalilore wa mau a Mulungu ndi kalilore weniweni ndi kunena kuti ‘Ndinawumbidwa moopsa ndi madabwitsa.’”

Ndipo mufike pafundo yakuti – uku ndi kumene kuli mphamvu zanga, izi ndi zimene zili zofooka zanga zimene ndi zopatsidwa ndi Mulungu. Umu ndi mmene Anandipatsira ine, koma zikhale momwe mukuganizira molondola za inu eni ake. Dziwani, “Musaganizire kwambiri mokweza inu nokha, musaganizire mozitsitsa kwambiri za inu nokha, koma kuganizira chiweruzo chodekha kapena cholondola. Ndiye kenako mau awa ochepawa. Dziwani kuti ikunena, “Malingana ndi mulingo wa chikhulupiriro chimene Mulungu wakupatsani inu”

Newell, mu ndemanga yake ya Aroma anaziyika bwino. Akunena kuti chikhulupiriro mmalo ngati awa sichikhulupiriro cha omvera. Sichikhulupiriro cha mwa Khristu; ndi chikhulupiriro. Akunena kuti ndi mulingo umene timadzisanthula ife tokha. Chikhulupiriro ichi ndi maonedwe a Baibulo a ife eni. Ndi amene inu muli mwa Khristu. Ndi mmene Mulungu wakupatsirani inu mphatso ndi kumvetsetsa malingaliro Ake a pa inu. Zili ngati ndime zitatu zoyamba za mitu ya Aefeso. Ndi chosowokera chanu kudziona inu eni ngati kuti ndi wokondedwa, ndinu wotengedwa, womatidwa ndi Mzimu. Muli ndi cholinga. Ndinu chimango chake. Chili chonse chimene muchisowa muli nacho mwa Khristu. Ndinu mwana wake wa mwamuna, ndinu mwana wake wamkazi, ndinu wokhululukidwa, ndinu wokondedwa. Ameneyo ndi amene inu muli. Ambiri mwa ife sitimaganiza choncho za ife eni ake. Chimenecho ndi chifukwa chake dziko lapansi liri ndi chikoka cha ife. Ndidzavomerezedwa, ndidzakhala ofunikira ngati ndingawoneke choncho, kapena ngati ndichite choncho kapena ngati ndingapange ndalama zambiri,

choncho kapena ngati anthu angaganize chonchi, kapena ngati ana anga angachite choncho. Ndipo ndi malingaliro olephera.

Choyambirira tikufunikira kuganiza molondola za ife eni tokha chifukwa ichi ndi mmene Mulungu akunena kuti ndife. Tonse timadziwa kuti anthu amaganiza zapamwamba kwambiri za iwo eni okha. Zoonza? Chimatchedwa kudzikuzi kapena kunyada. Ndipo inu mukudziwa amakhala ngati kudzitsekera, 'Kodi mwawona nsapato zanga zatsopano? Mukudziwa ndinali ku Nordstrom tsiku lina.' Kapena "Mukudziwa, ndimangodana nazo pomwe ndimakhala otanganidwa kwambiri nthawi ino ya pa chaka ku zisumbu za Greek, mukudziwa? Wa malonda wa Lexus andipatsa mpishumpishu. Ndinali wokhumudwiratu ndi galimoto imeneyo. Mukudziwa, ndikuganiza zogula Bentley nthawi ina."

Pamenepa, Izo zinali zisonyezo zongoseketsa. Ndikhulupirireni ine, tinapeza njira ya mmene timachitira chinthu chomwecho muuzimu ndi ndime ndi kungoyimanso chomwecho. Koma zimenezo zitha kukhala zotsutsa kwambiri. Kotero sidikufuna kupita kumeneko koma tonse takhala pakati pa anthu amene ali ndi chipambano chotero. Ndipo chili chonse cha mwa inu chikutt, "Sindikufuna kukhala pafupi ndi munthu ameneyo." Amaganiza kwambiri za pamwamba za iwo wokha. Koma molondola ndi anyamata ang'ono a mantha kapena atsikana ang'ono amene amaopa simudzawakonda nkomwe, iwo ndipo ophunzira mmene angabisalire.

Ndipo pali anthu ena amene amadzitsitsa okha. Mulungu sangandigwiritse ine ntchito. Ndine wopanda phindu. Ndikudziwa kuti Baibulo limati pali mphatso, koma Mulungu anadutsa mu mtundu wonse wa anthu ndipo anabwera kwa ine ndi kunena kuti, "Oho, ndinathawa," Ndiliba mphatso ili yonse, ndiliba phindu lililonse. Ngati mukadadziwa kumene ndikochokera, palibe chiyembekezo pa ine. Tsopano imvani izi: ngati mungaganize zodzikuzi nokha kapena kudzitsitsa nokha, mukuganizira ndani? Inu. Mukuwona, kudzichepetsa sikuganizira modzikweza kwa inu nokha kapena kuganiza zozitsitsa kwambiri. Kudzichepetsa sizodziganizira inu panokha nkomwe. Mtumwi Paulo akuti, "Ganizirani ena angati ofunikira kwambiri kuposa inu eni ake.

Zikundikumbutsa ine kuti, sindinachite zambiri za izizi. Koma ngati munapangapo masewero a bowling, nthawi zina ndimakasewera bowling, osati kawirikawiri, mwina ngati kamodzi pa zaka zitatu kapena zinayi zili zonse. Mukudziwa anthu a pa TV amakhotsa bowling bwino, choncho ndidzayesera kukhotsa. Ndachita kafukufuku pa ichi ndingatse kuwukhotetsa kumanzere. Mongopanga moyesa, ndi mapini angati, ngati mungakhotsere kumanzere kwa ngalande, mumapeza? Zero. Chabwino, kenako ndiyesera ndi kubwezera kwambiri ndipo ndimayesera ndi kuponyera kumanja, ndipo umapita ku ngalande ya kumanja ndi mapini angati amene mumapeza?. Onani,

ziliba kanthu ngati mukuganiza modzikweza kwambiri kapena ngati mukuganiza modzitsitsa kwambiri. Mumaphonya. Iyo ndi mipira ya mungalande.

Mulungu amalamula – mongodziwabe ili ndi lamulo. Akulamula inu ndi kulamula ine kuganiza molondola, momveka, mu Baibulo kuti inu ndi ndani. Kukuyamba ndi kumvetsetsa lamulo limenelo, ndipo kenako umayamba ulendo ndi dongosolo lakukonzanso mtima wanu chifukwaa anthu ndi wofalitsa nkhani ndi dziko lapansi akukuwuzani inu kuti ndinu ndani mmoyo wanu wonse, ndipo inuyo muyenera kuphwanya zimenezo. Ndipo mumati, “Chabwino, chifukwa chiyani zili zofunika kwambiri?” Chifukwa ngati simumvetsetsa amene inu muli, simudzamvetsetsa mbali imene inuyo muli.

Dziwani ndime yotsatirayo, ndime 4 ndi 5 zikuti, “Pakuti monga mthupi liri limodzi,” kuyankhula za thupi lenileni, “tili nazo ziwalo zambiri.” monga maso ndi manja ndi mapazi ndi zina zambiri, ndipo ziwalo zonsezi siziri nayo ntchito imodzimodzi, chomwecho ife ndife ambiri, tiri thupi limodzi mwa Khristu ndi ziwalo zinzache, wina ndi wina”. Tsopano, mu zolembe zanu pamwamba “monga ngati” ndikufuna mulembe mawu akuti F.O.R. Pali mawu oyamba mu chi Greek pomwe abwera amatanthauza “chifukwa”.

Ndiponso, pofewetsa kumasulira nthawizina, “monga ngati” amamveka bwino, koma chifukwa chimene akunenera chifukwa ndi kuti mumvetsetse kuti inu ndi ndani ndikuganiza molondola za inu ndi zanu basi, monga ngati thupi la munthu lili ndi ziwalo zambiri ndipo zonse sizigwira ntchito mofanana Chonchonse ife amene tili ambiri ndi thupi limodzi mwa Khristu ndipo inu mumakwanir. Ndipo ngati simukudziwa – ngati simunadziwe munali diso, simukanadziwa pamene mukukwanira. Ngati mulibe kudziwunikira kwanokha kodekha simungadziwe mbali imene inuyo mumakwanira.

Koma pano pali chimene akunena. Mongoyerekeza zalazi izi kutuluka ngati chonchi ndi mphamvu zanu. Mulungu amakupatsani mphamvu zimene zimamanga chidaliro chanu ndi kukulolani inu kumvetsetsa kuti muli ndi zopereka za paderadera zothandizira anthu ena. Tsopano timakhala mdziko limene sitienera nkomwe kukhala ndi zofooka, ndiye choncho timalewa kunama, kukana, kunyengezera.

Koma Mulungu anapereka zofooka kuti apange kudalira ndi kudzichepetsa kotero kuti pakhale kudalirana, choncho kuti zolimba za anthu ena zikumane ndi zofooka zanu, kotero kuti akuchitireni inu zimene zimungathe kuchita panokha. Mumasowekera anthu. Kodi mukudziwa chimene zimenezo chimatenga? Kudalirana kapena kudzichepetsa, ndipo zimalenga kukongola.

Ntchito yanu ndi kuganiza ndi kupempherera za zinthu zitatu zoyambirira za mbali ya mphamvu zanu. Osati zimene anthu amaganiza, osati zimene inu mmaganiza koma zimene Mulungu akunena. Mwina mwake mupite kwa anthu ochepa amene muli nawo pafupi amene amakhudziwani bwino amene angakuuzeni zoon. Ena mwa ife timafuna kulemba zamphamvu zathu chifukwa timaganiza kuti zingatipange ife kukhala wina wake, koma mbali ya mphamvu zanu ndi chiyani? Uwu ndi ulendo.

Ndipo kenako molondola lembani zinthu zitatu zoyambirira za mbali ya zofooka zanu. Ndipo pomwe mwapeza zimenezo, chimene mumvetsetse ndi, mmalo mothamphamvu zonse izi kudzipisa ndi kumachita ngati mulibe, mudzangozindikira kuti izo ndi maitano a Mulungu amene anakulengani inu kulola anthu ena abwere mmoyo mwanu ndi kukukondani inu mnjira imene mmumayisowokera kwambiri.

Pomwe ndinali mbusa, ndinali ndi ana awiri kukoleji nthawi imodzi, ana awiri anali masukulu a Chikhristu, ndipo pa zenera limenelo la nthawi, ndikukumbukira kuwerenga pepala. Santa Cruz anali malo odula kwambiri kukhalako mu America kuposera mzinda wa New York, kuposera San Francisco, ndipo zinali zosokonekera. Ndiye kungoyesera kuti zigwire kunali kovuta kwambiri

Ndipo choncho pamene china chake chaonongeka mnyumba mwathu, kuyitana munthu wodzakonza sizinali zosankha. Ndinalibe ndalama zina zili zonse zoyitana munthu wokonza. Ndiye panali mkulu wa mpingo mutchailitchi wotchedwa Dick. Anali munthu waumulungu, mphunzitsi wopuma pa ntchito. Amatha kukonza chili chonse. Tinagula nyumba yakalekale imene inasowokera kukonza zinthu zambiri. Kukagwa mvula, mvula imalowera pa zenera lina, ndi nthawi zonse zimene tayatsa makina otsukira mbale amadontha. Zimamukwiyitsa mkazi wanga kwambiri, koma tinangoyika nsalu pansi pa makina otsukira mbale kotero kuti izilandira madzi ndipo kenako ndikutulutsa mbale. Zinaoneka ngati zikugwira kwai ne, koma iye sanaganize kuti limenelo linali dongosolo labwino.

Ndipo choncho Dick amabwera, ndi pa tsiku langa lopuma mwa masabata ambiri, Dick ndi ine timatha kukonza zinthu chimene chikutanthauza kuti ndimayendetsa kupita ku Home Depot ndi Dick, ndinagula zida, ndiye kenako ndimagwada pansi pafupi ndi Dick ndi kumamupatsira zida ndi kumufunsa mafunso ochepa. Ndipo mapeto ake anati, “Chip, simudzadzimvetse mnjira iliyonse, komabe ndi zabwino.”

Ndinaphunzira zambiri kukhala munthu wa Mulungu – anali ndi ana akulu, anali wamkulu ndi za 20 kuposa ine – zokhudza kukhala bambo wa ana ndi za mmene ungakhalire mbusa kuchokera kwa Dick kuposera munthu wina aliyense mu tchalitchi chimenecho, chifukwa? Chifukwa ndinali ndi chosowa. Sindingathe kukonza

chilichonse. Moonadi sindingakonze chilichonse, iPad inabwera ndimavuitika kuti ndigwiritse ntchito iPad sindine wazamanja, koma chosowa chimenecho chinalenga ubale.

Kodi chimene chingachitike ndi chiyani mutakumana ndi inu weniweni. Chotsani chigoba chanu cha chionetsero ndi **hologram** ndi kuzindikira kuti Mulungu akufuna kubweretsa anthu mmoyo mwanu? Ndipo nanga bwanji mutachotsa kudzichepetsa kwabodza ndi kuzindikira kuti ena mwa inu ndinu anthu abwinokwambiri pa zinthu zina mmalo mungonena kuti, "Chabwino, mukudziwa, sindikufuna kunena chili chonse monga, ndimachita bwino pa icho." Chifukwa angaganize kuti ndikuyesera kukhala onyada." Angathe mwina kuganiza kuti mukuyesera kuwakonda iwo. Ndipo tonse monga thupi tibwera pamodzi. Ndi chipangidwe cha Mulungu. Ndi cha mphamvu. Ndi chokongola. Ndi chodabwitsa.

Ndipo, mukudziwa, izi sizingachitike pobwera ku tchalitchi – ngakhale zili zokondweretsa ngati mmene zilili kubwera ku tchalitchi- ndi kukhala pa dongosolo la mapemphero nd kukhala otha kutenga nawo gawo pang'ono. Chimene ndangochifotokozachi sizingachitike pokhapokha mutachulumikizana mwaubale, ndi anthu amene mukuwadziwa, ndi kupita kukawamasula, ndi kutenga masitepe awo a ukhanda a kudalira.

Ndipo chifukwa chimene magulu ang'ono ali ofunikira kwambiri ndi chakuti ndi chotengera chimene mudzi weniweni ungchitikire. Kukhala mgulu laling'ono sikungakupangitseni inu kuzama muubale, koma ndi chotengera kawirikawiri chimachitika kumene inu mumagawa moyo wanu weniweni ndi mtima wanu.

Ndiye choncho inu ndi ndani. Mukusowokera kuganiza molondola za inu eni mmene Mulungu amakuwonerani inu. Chifukwa? Chifukwa muli ndi mbali yakuti mukwaniritse ndipo simungadziwe udindo umenewo pokhapokha ngati mutadziwa kuti inu enieni ndi ndani.

Ndiye kenako mudzanena, 'udindo wake uti? Pamene ndikukwanira ndi pati? Ndiwonetseni Mulungu.' Iye adzanena kuti "Ndasungitsa mwa iwe mphatso ya uzimu yoyamba," muli okonzeka. "mphatso ya uzimu yoyamba ndikuchita zinthu zambiri zosiyanasiyana, koma ndikufuna kuti ine mutenge gawo lalikulu kwambiri la mphamvu za mthupi la Khristu ndi kulunjika pamenepa."

Yang'anani chimene Paulo akunena pa ndime 6 mpaka 8. Kodi mukuyenera kuchita chiyani? Akunena kuti tili ndi mphatso zosiyanasiyana molingana ndi chiyani? "Monga mwa Chisomo chapatsidwa kwa ife." Koteri ndi zopatsidwa ndi Mulungu. Palibe malo

onyada. Kenako akuti, “Kapena mphatso yakunenera tinenere, monga mwa muyeso wa chikhulupiro. Kapena yakutumikira tidzipereke ku utumiki uwu; kapena iye wakuphunzitsa, kukuphunzitsako, kapena iye wakudandaulira, kukudandaulirako, wakugawira achite ndi mtima woona, iye wakuweruza, aweruze ndi changu; iye wakuchita chifundo, achite ndi kukondwa mtima.

Mfundo ya ndime iyi sikutokoza mphatso. Kodi mfundo ndi itii? Ngati munapatsidwa kuphunzitsa, osafunsa mafunso a ndale, kodi mukuyenera kuchita chiyani? Phunzitsani. Ngati mwapatsidwa kulangiza ndi kulimbikitsa, kodi mukuyenera kuchita chiyani? Tabwerani. Ngati mwapatsidwa kutsogolera, tsogolerani molimbika. Zooni? Mfundo ndi yakuti kuli zinthu zambiri zimene mungachite.

Munapatsidwa ndipo muli ndi china chake chapaderadera chobweretsa kuthupi la Khristu. Umu ndi mmene mumapangira masanjidwe a kumene mungathere nthawi yanu ndi moyo wanu ndi mphamvu zanu ndi zinthu zanu zoyambirira zofunika. Simuyenera kupezeka ku bungwe lililonse ndi kuthandiza chilichonse mmudzi ndi china chilichonse pena paliponse nthawi zonse. Mukusowekera kukhala ndi masanjidwe. ‘Izi ndi zimene ndili nazo mphamvu, izi ndi zofooka zanga, iyi ndi mphatso yanga yoyambirira ya uzimu, izi ndi zinthu zanga zoyenera kuchita moyambirira, iyi ndi nyengo ya moyo wanga imene ine ndili...chabwino, Ambuye, ndiyikeni pa mzere. Ndipo mukachita choncho, mudzazindikira mbali imene munazama ndipo mudzachita chimene anakupangirani inu muchite.

Ndipo choncho choyeserera pano, kuika mophweka kwambiri ndi kutukira ndi kugwiritsa ntchito mphatso zanu zauzimu. Muyankha mafunso awa poganizira molondola za inu eni ake, kukhala ndi kulumikizidwa kwa ubale, ndipo kutulikira ndi kugwiritsa ntchito mphatso zanu za uzimu. Ndikufuna kukukumbutsani inu, nthawi zina mungathe kukumba kwambiri mmafundo awa, koma kumbukirani ziimene Yesu ananena? Uzimu weniweni ndi kugonjera kwa Mulungu, kudzipatula ku dziko lapansi ndi kudzisanthula kodekha.

Zimenezo ndi zazikulu kwambiri, koma zonsezo ndi chiyani? Zimenezo ndi mbiri chabe kotero kuti mukonde Mulungu ndi mtima wanu wonse, ndi moyo wanu wonse, ndi nzeru zanu zonse, ndi mphamvu zanu zonse. Mumakonda ena monga mmene mukuphunzirira kuyamba kuyamikira ndi kukonda inu. Ndipo simudzakonda inu mpakana mutayamba kukumbukira ndi kugwira mmene Mulungu amakuonerani inu, osati mmene inu mumadzionera, osati mmene amayi anu amakuwonerani, osati mmene abambo anu samapezekera kapena sanakuwoneni inu, osati mmene anzanu atanga limodzi amakuwonerani inu.

Pali zinthu zitatu zimene ndikufuna kuti musadzayiwale, chabwino? Mukhoza kuyang'ana ndime. Izi ndi zimodzi ngati ndikadakhala inu, ndikaloweza. Moona ine ndinaloweza. Ndikufuna musadzayiwale nkomwe amene weniweni inu muli. Masalmo 139 akuti Mulungu mwapaderadera anakulengani inu. Ndinu wofunika wamuyaya. Ndinu wopangidwa moopsa ndi modabwitsa. Ndime iyi idzapitilira ndi kukamba za mmene inu munali mmimba mwa amayi anu mmene munkawumbidwa mchibelekeri ndi Mlengi wa dziko lonse lapansi chifukwa lye anali ndi malingaliro a inu ndipo anakupangani wopatulika monga mmene inu mulili. Ndipo sakukukondani kokha, mwakonzekera izi, Mulungu amakonda inu. Ndimakumana ndi anthu nthawi zonse amene anatsimikizira, 'Oh, ndikuganiza kuti Mulungu amakonda ine, sindikungoganiza kokha kuti amakonda ine.' Amakunyadirani inu. Amakuyimbirani inu.

Chinthu chachiwiri chimene musadziyiwale ndi chakuti anakuyikani inu mbanja Lake. Ndinu wovomerezedwa opanda zoyenereza. Mu Aefeso 3, Paulo akupemphera, "Mukakhosetu kuzindikira pamodzi ndi oyera mtima onse, kupingasa ndi utali, ndi kukwera ndi kuzama mchiyani ndi kuzindikira chikondi cha Khristu." Amakukondani. Amakukondani osatengera kumene inu mumakhala, osatengera zimene zakuchitikirani. Chifukwa cha ntchito ya Khristu pa mtanda, imfa yake imene inalipira ndi kukwirira machimo anu, ngati muli otsatira wa Yesu, anakuwombolani inu ndipo lye amakukondani inu ndipo lye amatenga machimo anu kutalika kwake ngati kuchokera ku mmawa kukafika ku madzulo. Inu ndinu chinthu cha chikondi chake. Ngati palibe wina aliyense amasamala za inu, lye amasamalira inu.

Ndipo chachitatu, musadzayerekeze kuyiwala kuti Mulungu anakupatsani kukwanitsa cholinga chake. Ndinu woyenera opanda olova mmalo mwanu. Ndinu woyenera. Inu ndinu chimango chake cholengedwa mwa Khristu Yesu. Aefeso 2:10 akuti, "Kuchita ntchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikayende mmenemo"

Pomwe mwaganiza molondola za inu nokha ndipo ndi ntchito yolimba, zidzakusinthani inu. Ngati muli okwatira, zidzasintha ukwati wanu. Ngati muli kholo, zidzasintha mmene mumalera ana anu. Izi ndi mtundu wa zinthu zimene mmachita ndi ana anu. Izi ndi mtundu wa zinthu zimene mmachita ndi zonse zokukakamizani, zimene zidzakonzanso mtima wawo – nthawi yogona pakama ndi pamene mukhala pa tebulo. Izi ndi zinthu za mtundu zimene mumachita ndi amene mmagawana naye chipinda kuzindikira kuti muyenera kukhala munthu wokhoza, osati kupeza munthu wokhoza. Ndipo pamene mwapeza maonedwe olondola a inu eni ake, inu ndi wokongola kwambiri, wowoneka bwino kwambiri, wopambana kwambiri pamaso pa dziko lapansi chifukwa palibe wofanana ndi inu.